Adatifera chifukwa if, adamuika m'manda ndipo anaukitsidwa kwa akufa patapita masiku atatu. Naweso ungathe kupulumutsidwa lero lino! *"Kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiyo Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapululmuka"* Aroma 10:9

Usakhale ngati chitsiru!
"Chitsiru chimati mumtima mwache, kulibe Mulungu…" Masalmo 53:1 Ngati uganiza bwino mumtima mwako ukhoza kubvomereza kuti Mulungu aliko chifukwa umboni umene uli ponse ponse, koma chikumbu mtima chilipo kuti Mulungu aliko ndipo tsiku likubwera pamene udzayankha pa maso pa lye. *"Kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi la za pa dziko, ndi za pansi pa dziko, ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Khristu ali Ambuye, kuchitira ulemu Mulungu Atate."* Afilipi 2:10-11

Hope tract ministry
All tracts are free, as the Lord provides

P.O. BOX 609 ● YORK, SC 29745 ● 803-684-1535
WWW.HOPETRACTS.ORG
If There Is A God (Chichewa) Tract 532

Ngati Kuli Mulungu, Chifukwa Chani Sadziwonetsera

Umboni woti kuli Mulungu uli ponse ponse, mwina ngati ndiwe m'modzi wa anthu amene akuti zinthu zinachitika mwa mwayi. Chimatengera chikhulupiriro chachikulu kukhulupirira kuti Mulungu ndiye analenga chilichonse osati munthu anachokera ku umoyo wina waung'ono kwambiri. Anthu ena amakhulupirira kuti umoyo umachokera ku zinthu zazing'ono ndipo zimakula. China chilichonse chimayamba mwadongosolo ndikuthera mwachisawawa (Yesaya 51:6, Masalmo 102:25-26, Ahebri 1:10,11)

Tiyeni tiyang'ane m'mene timakhalira mu dziko mwathu, tiwona kuti anthu akupanga zachiwembu, upandu ndi nkhanza chaka chilichonse. Dziko lapansi likutha ndi zizindikiro zikupitilirabe kuchitika, njala ndi zibvomezi ndi ngozi zachilengedwe. (Mateyu 24:3-8, Luka 21:10,11)

Anthu a sayansi akulephera kuvankha funso la kale ili, "Pakati pa dzira ndi nkhuku chinayamba ndi chiyani?" Mulungu akuti adalenga china chili chonse chamoyo. (Genesis 1:21-25)

Mulungu amadzibvumbulutsa kwa ife m'njira zambiri:

Iye amadzibvumbulutsa kudzera mu chilengedwe Chache. *"Pakuti chilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zache ndizo mphamvu yache yosatha ndi umulungu wache, popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula."* Aroma 1:20. Mulungu akuti umboni waonekeratu kudzera mu zonse adadzilenga ndipo Iye sadzalora chowiringula pa tsiku la chiweruzo. Kunene kuti umakhulupirira kuti Mulungu kulibe komanso sumakhulupirira mu mphamvu yache zimenezi sizidzapindula kanthu pa tsikulo. *"Zakumwamba zimalalikira ulemero wa Mulungu, ndipo thambo lionetsa ntchito ya manja ache. Usana ndi usana ukuchurukitsa mau, ndipo utsiku uonetsa nzeru."* Masalmo 19:1,2

Iye amadzibvumbulutsa kudzera mu mau Ache.
Panopa munthu sanganene kuti Mulungu kulibe iyeyo anadzibvumbutsa zaka zikwi zapitazo munjira zina. Iye adalankhula momveka bwino kwa anthu ena, ndiponso kudzera mwa aneneri koma kudzibvumbulutsa kwakukulu kudakwaniritsidwa kudzera mwa Mwana Wache, Yesu Khristu. "Kale Mulungu analankhula ndi makolo mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyanasiyana, koma pakutha pache pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe." Ahebri 1:1-2. Pa nthawi ino pamene tili ndi Buku Lopatulika, Mulungu sagwiritsaso ntchito aneneri. Mulungu akufuna ife kuti tidziwe mau ache ndi kuwasunga.

Iye amabvumbulutsa uchimo wathu kudzera mu lamulo Lache. *"Komatu lembo linatsekereza zonse pansi pa uchimo, kuti lonjezano la kwa chikhulupiriro cha Yesu Khristu likapatsidwe kwa okhulupirawo, momwemo chilamulo chidakhala namkungwi wathu wakutifkitsa kwa Khristu, kuti tikayesedwe olungama ndi chikhulupiriro."* Agalatiya 3:22,24. *"Pakuti kulibe wolungama pansi pano amene achita zabwino osachimwa."* Mlaliki 7:20. Iye amadzimbulutsa chiyero chache kudzera mu chilango cha uchimo.
"...moyo wochimwawo ndiwo udzafa." Ezekieli 18:4
"Pakuti mphotho yache ya uchimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Khristu Yesu Ambuye wathu." Aroma 6:23

Iye amadzibvumbutsa chikondi chache kudzera mu imfa pa mtanda. "Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chache cha mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu adatifera ife" Aroma 5:8.